



(CHICHEWA)

# NJIRA YA KASAMBIDWE {KUSAMBA}



Lamasulidwa  
m'chichewa ndi

Oyambitsa  
Sheikh-e-Tariqat Amir-Ahl-e-Sunnat II fondatore di  
Dawatulislami Allama Maulana Abu Bilal  
**MUHAMMAD ILYAS**  
Attar Qadiri Razavi

غُسل کا طریقہ (شافعی)

Njira ya kasambidwe ya (Shafi'i)

## Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

Kabukuka kaperekedwa m'chiyankhulo cha chi Urdu ndi Majlis Al-Madinah-tul- 'Ilmiyyah. **Nthambi Yomasulira ya** (Dawat-e-Islami) yamasulira bukuli m'Chicewa. Ngati mungapeze cholakwika chilichonse pakumasulira kapena malemba, chonde dziwitsani Nthambi Yomasulira podzera pa keyala iyi kapena pa keyala ya E-mail ndi cholina cholandira mphotho [Sawab].

### Nthambi Yomasulira (Dawat-e-Islami)

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran,  
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

**UAN:** ☎ +92-21-111-25-26-92 – Ext. 7213

**Imelo:**  [translation@dawateislami.net](mailto:translation@dawateislami.net)

## Njira ya Kasambidwe ya (Shafi'i)

Kumasulira m'Chichewa kwa 'Njira ya kasambidwe ya (Shafi'i)'



### UMWINI ONSE NDI OTETEZEDWA

Ufulu wokopera © 2024 Maktaba-tul-Madinah

---

Palibe gawo lililonse labukuli limene lingazasindikizidwenso kusungidwa mukachitidwe kochulutsa kapena kufalitsa mwa maonekedwe aliwonse kapena mwanjira iliyonse ,kudzera mzamagesi, makina, kujambula kapena mwinamwake popanda chirolezo cholemba kuchokera ku Maktaba-tul-Madinah.

**Kusindikiza koyamba:** Shawwal-ul-Mukarram, 1445 AH – (May, 2024)

**Lomasuliridwa ndi:** Nthambi Yomasulira ya (Dawat-e-Islami)

**Wosindikiza:** Maktaba-tul-Madinah

**Kuchuluka:** -

#### **Thandizo**

Chonde khalani omasuka kutiyankhula ngati mukufuna kuthandizira kusindikiza buku lachipembedzo kapena ka buku kuti likhale Isal-e-Sawab ya abale anu omwe anamwalira.

#### **Maktaba-tul-Madinah**

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah Mahallah Saudagran,  
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

 **E-mail:** maktabaglobal@dawateislami.net – maktaba@dawateislami.net

 **Lamya:** +92-21-34921389-93

 **Webu:** [www.dawateislami.net](http://www.dawateislami.net)

الْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى خَاتَمِ النَّبِيِّنَ  
أَبَأَبَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيمِ يٰسُوْلِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيمِ

## Du'a Powerenga Buku

Werengani Du'a yosatirayi (pempho) musanayambe kuwerenga buku kapena phunziro la Chisilamu mudzakumbukira chilichonse mwaphunzira, لِن شَاءَ اللّٰهُ:

اللّٰهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَانْشُرْ  
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْإِكْرَامِ

## Kumasulira

E Allah ﷺ! Titsegulireni makomo a chidziwitso ndi nzeru, ndipo tichitireni Chifundo! E, inu Amene muli Waulemerero komanso Wolemekezeka Kwambiri ! (*Al-Mustatraf*, vol. 1, p. 40)

## Dziwani:

Mfunireni zabwino Mtumiki ﷺ kamodzi kumayambiriro komanso kumapeto a Du'a.

# M'ndandanda wazamkatimu

Chonde poyamba werengani izi .....	1
Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i) .....	3
Kupambana kotumiza Mtendere ndi Madalitso kwa Mtumiki ﷺ .....	3
Chilango chachirendo.....	3
Njira ya Kasambidwe ya (Shafi) .....	5
Zikakamizo ziwiri za kusamba .....	7
1.      Chitsimikizo .....	7
2.      Kuthira madzi thupi lonse .....	8
Machenjezo 20 kwa amuna ndi akazi panthawi ya kusamba.....	9
Machenjezo anayi kwa akazi.....	11
Malamulo okhudzana ndi bala lomangidwa .....	12
Zifukwa zisanu zopangitsa kusamba (ghusl) kukhala (fardh) chikakamizo ...	13
Kufotokoza kofunikira kokhudza magazi pambuyo pobereka.....	14
Malamulo Atatu Ofunika .....	15
Chilango chodziseweretsa maliseche.....	16
Ndi nthawi iti pamene kusamba kuli Sunnah? .....	17
Zitsimikizo zingapo mukusamba kumodzi .....	19
Kusamba pamvula .....	20
Malamulo asanu ndi anayi okhudzana ndi kuwerenga kapena kukhudza Quran Yopatulika munthu ali ndi unve wa ukulu.....	21
Kugwira mabuku achipembedzo opanda wudhu.....	23
Kufunira mtendere ndi madalitso (salat) kwa Mtumiki okondedwa pamene munthuyu ali mu umve.....	24
Kodi ndi nthawi iti yomwe mwana amakhala wamkulu? .....	24
Kodi mabuku ayenera kusungidwa mu ndondomeko yotani?.....	25
Kuyika ndalamu kapena zinthu zina mkat i mwa pepala lomwe lili ndi zolemba zachipembedzo.....	26

Chiyambi cha manong'onong'o a satana.....	26
Tayammamu.....	27
Ntchito zokakamizika ( <i>faraidh</i> ) za <i>tayammamu</i> .....	27
Zochita 19 za ma Sunnah pa tayammamu.....	28
19. Kupemphera ma (rakah) awiri a Swalah pambuyo pa <i>tayammamu</i> ....	30
Njira za <i>Tayammamu</i> (Shafi'i) .....	30
Ngale 25 za Madani zokhudzana ndi Tayammamu.....	32
Malangizo a Madani.....	38
Mukamaliza kuwerenga kabukuka, perekani kwa ena mokoma mtima .....	38

## Chonde poyamba werengani izi

الحمد لله Dawat-e-Islami ndi Bungwe lachipembedzo lomwe lili ndi odzipereka a Mtumiki. Muyambitsi wa bungweli, Ameer Ahlus Sunnah, ‘Allamah Maulana Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadri Razavi Ziyai دَاعِثٌ بِرَحْمَةِ الْعَالِيَّةِ walemba mabuku osiyanasiyana okhudza mitu yambirimbiri yosiyansiyana. Nkhani za m’mabuku amenewa zili zokhudza chiphunzitso (aqeedah), ntchito zabwino ndi zoipa, mbiri ya anthu otchuka, shari’ah, uzimu, mbiri, sayansi, mankhwala, kukonza chikhaldwe, makhalidwe, zochitika za tsiku ndi tsiku ndi zina zambiri. Mabuku ake amapanga chuma chamtengo wapatali cha maphunziro ndi nzeru zamtengo wapatali.

Pachifukwa ichi, Nthambi ya mabuku a Fiqh Shafi’i ya al-Madinah al-Ilmiyyah (centa yofufuza ya chisilamu) ikukonzanso zolemba za Ameer Ahlus Sunnah دَاعِثٌ بِرَحْمَةِ الْعَالِيَّةِ - molingana ndi ganizo la chiphunzitso cha Shafi’i. Izi zikuchitika pofuna kuperekwa mwayi kuti amene amatsatira sukulu ya kaganizidwe ka Shafi’i apindule ndi ngale zanzeru zoperekedwa ndi Ameer Ahlus Sunnah دَاعِثٌ بِرَحْمَةِ الْعَالِيَّةِ.

- ❖ Malamulo a fiqh omwe atchulidwa m’bukuli asinthidwa molingana ndi Malamulo ochokera m’mabuku odalirika a sukulu ya Shafi’i.
- ❖ Zowonjezera zofunika za ikidwamo.
- ❖ Pokonza zosinthazi, kulemekeza kwaperekedwa ku mawu

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

a Dawat-e-Islami, centa yofufuza ya chisilamu ndi mfundo zaposachedwa za Nthambi ya mabuku a Fiqh Shafi'i.

- ❖ Pomaliza ntchito zomwe tatchulazi, Mufti Muhammad Rafeeq Sa'eedi al-Shafi'I مفتی محمد رفیق سعید الشافعی anaunikanso kabuku konse mogwirizana ndi mfundo za Chisilamu.
- ❖ Ubwino uliwonse umene ukupezeka m'kabukuka ukuchokera m'chisomo cha Allah Wamphanvu zonse, kuwalowa manja kwa Mneneri wake womaliza صلی اللہ علیہ وسّلّمَ, kupereka kwa oyera mtima olemekezeka ndi mapemphero owona mtima a Ameer Ahlus Sunnah دامت برکاتہم العالیۃ. Zolakwika zilizonse zili kumbali yathu.

Al-Madinah al-Ilmiyyah (centa yofufuza ya chisilamu),  
Nthambi ya mabuku a Fiqh Shafi'i

4 Rajab al-Murajjab, 1442AH (17 Febuluwale 2021)

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

الْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى خَاتَمِ النَّبِيِّنَ  
أَمَّا بَعْدُ فَاعُوذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطَنِ الرَّجِيمِ يٰسُمُ اللّٰهُ الرَّحْمٰنُ الرَّحِيمُ

## Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

Kupambana kotumiza Mtendere ndi Madalitso kwa  
**Mtumiki** صلوة العاذرة

Mtumiki Wokondedwa حَلَى اللّٰهِ عَلٰيْهِ وَالْمَسَكَنُ anati: “Ndifunireni zabwini ine mochuluka; ndithudi, kutero ndiyе kuyeretsedwa kwanu.”<sup>1</sup>

صَلٰوةُ اللّٰهِ عَلٰى مُحَمَّدٍ      صَلٰوةُ عَلٰى الْحَكِيمِ

### Chilango chachirendo

Sayyiduna Junaid al-Baghdadi حَمَّةُ اللّٰهِ عَلٰيْهِ akunena kuti Ibn al-Kuraybi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلٰيْهِ anati: “Nthawi ina, ndinadzilotera usiku, ndiyе ndinapanga chitsimikizo chakuti ndisambe nthawi yomweyo. Popeza unali usiku wozizira kwambiri, Mtima wanga unasonyeza ulesi ndi kunena kuti, ‘Nthawi ikanalipo yaitali ya usiku. Ukufulumira ndi chiyani? Uckoza kusamba kochotsa litsiro lalikulu m'bandakucha momasuka. 'Nthawi yomweyo ndinalumbira kuperekira chirango chachirendo kwa Mtima wanga posamba nthawi yomweyo nditavala zovala

<sup>1</sup> Musnad Abi Ya'la, vol. 5, p. 62, Hadith 6407

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

ndikuwumitsa zovala pathupi langa nditamaliza kusamba popanda kuzifinya. Ine ndinachita zimenezi. Ndithu, Mtima wosamvera umene uchita ulesi kutsatira malamulo a Allah uyenera kulangidwa motere.”

Allah Wamphanvu zonse amuchitire chifundo iye ndi kutikhululukira ife popanda kuwerengeredwa ntchito chifukwa cha iye.

اُمِّيْنِ بِجَاهِ الْخَاتَمِ النَّبِيِّنَ ﷺ

صَلَوَاتُ اللَّهِ عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Okondedwa awerengi, mwa wona momwe anthu owopa Mulungu akale ﷺ anali kupirira kuzowawa kuti alepheretse zolina zoipa za Mtima! Fanizo lomwe takambiranali lili ndi phunziro lalikulu kwa abale omwe akumana ndi vuto la kudzilotera usiku, iwo amaphonya Swalah ya Fajr yapagulu kapena, Allah aletse, ngakhale kuphonya Swalah yonse chifukwa cha ulesi kapena kuchita manyazi (kupanga kusamba pamaso pa abale awo). Anthu otete samalabadira za manyazi owopsa a Tsiku lomalidza. Nthawi zonse kusamba kukakhala fardh, munthu azisamba mofulumira nthawi ya Swalah ikafika. Hadith imati: “Angelo salowa m'nyumba momwe muli chithunzi, Galu kapena junub (munthu amene kusamba kuli kokakamizika kwa iye chifukwa

cha kugonana, kapena kutulutsa umuna chifukwa cha chilakolako).<sup>1</sup>

### Njira ya Kasambidwe ya (Shafi)

Ndi Sunnah kuti *junub* achite *istinja* asanasambe kuti umuna uliwonse wotsala uchoke m'thupi. Pamene mukutsuka ziwalo za *istinja*, ndibwino kupanga chitsimikizo kuchotsa zonyansa m'ziwalo ziwigizo, chifukwa kukhudza ziwalozo pa nthawi ya kusamba kumawononga wudhu. Kenako munthu amene akukakamizika kusamba apange chitsimikizo chotsatirachi: **بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ**<sup>2</sup> (Ndikupanga chitsimikizo chofuna kusamba kokakamizika). Pamene mukupanga chitsimikizo chimenechi, muyenera kuwerenga tasmiyyah kutanthauza kuti **بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ**<sup>2</sup> uku mukusambisa manja onse awiri mpaka molekezera zikhato, ndipo ngati pali chodetsedwa paliponse m'thupi, chiyenera kuchotsedwa.<sup>3</sup> Kenako, m'kamwa mutsukidwe motsatizana ndi kukwezera madzi m'mphuno. Kenako, wudhu wonse wa pa Swalah uchitike. Pambuyo pake, onetsetsani kuti madzi afika mbali zonse za thupi zomwe ndi mopindika monga khutu, kukhwapa ndi mchombo. Tsatirani izi ndikunyowetsa zala za manja onse awiri ndikuchita khilal yamizu ya tsitsi katatu. Tsopano, thirani madzi pamutu katatu,

---

<sup>1</sup> Abu Dawud, p. 50, Hadist 227

<sup>2</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 129-134

<sup>3</sup> al-Manhaj al-Qaweem, p. 117 Njira ya kasambidwe ya (Shafi'i)

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

kenako paphewa la kumanja katatu, kenako paphewa lakumanzere katatu, kenako pathupi lonse katatu. Ndi Sunnah posamba kuyang'ana ku qiblah komanso mosalekeza. Sambani poyendetsa dzanja pathupi lonse ndikulisisita. Ndi Sunnah kusunga chitsimikizo cha kusamba ndikukhala mu wudhu mpaka kusamba kutakwanira. Munthu ayenera kusamba pamalo pomwe anthu ena sangamuwone. Ngati malo oterowo palibe, mwamuna ayenera kuphimba *satr* (malo oyambira pam'chombo mpaka m'mawondo) ndi nsalu yokhuthala. Ngati palibe nsalu yokhuthala, kulungani nsalu ziwiri kapena zitatu zopyapyala pa *pobitsika*, popeza nsalu (Imodzi) yopyapyala imamatirira pathupi ndi kuwonetsa poyer a mtundu wa ntchafu ndi mbali zina zathupi (Allah aletse).

Munthu wamkazi ayenera kusamalitsa kwambiri. Dzivani kuti ndizololedwa kwa munthu kusamba payekha atavula, ngakhale kuti ndi bwino kuphimba malo obisika. Sizoyenera kulankhula panthawi yosamba, ndipo musapukute thupi lanu ndi thaulo popanda chifukwa chomveka.<sup>1</sup> Valani zovala nthawi yomweyo mukamaliza kusamba.

Mukamaliza kusamba, muli chiyang'anire ku Qiblah, kwezani manja anu ndikuyang'ana kumwamba ndikuwerenga izi katatu:

---

<sup>1</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 129-135

أَشْهُدُ أَنَّ لِلَّهِ إِلَّا اللَّهُ وَحْدَهُ لَا شَرِيكَ لَهُ وَأَشْهُدُ أَنَّ مُحَمَّدًا عَبْدُهُ وَرَسُولُهُ اللَّهُمَّ اجْعَلْنِي مِنَ الشَّوَّابِينَ  
وَاجْعَلْنِي مِنَ الْمُتَطَهِّرِينَ وَاجْعَلْنِي مِنْ عِبَادِكَ الصَّالِحِينَ سُبْحَانَكَ اللَّهُمَّ وَبِحَمْدِكَ أَشْهُدُ أَنَّ لِلَّهِ إِلَّا  
أَنْتَ أَسْتَغْفِرُكَ وَأَتُوبُ إِلَيْكَ وَصَلَّى اللَّهُ عَلَى سَيِّدِنَا مُحَمَّدٍ وَعَلَى الْأَئِمَّةِ وَصَحْبِيهِ وَسَلَّمَ

Kenako werengani Surah al-Qadr katatu.<sup>1</sup>

## Zikakamizo ziwiri za kusamba

1. Chitsimikizo (Niyah).
2. Kupanga madzi kuyenda pa thupi lonse mowoneka.<sup>2</sup>

### 1. Chitsimikizo

- ❖ Amene ali pa chikakamizo chosamba, achite chitsimikizo chofuna kudziyeretsa ku nyansi zazikulu, ku msambo kapena kutuluka magazi pambuyo pobereka, kapena achite chitsimikizo chokwaniritsa kusamba kokakamizika.<sup>3</sup>
- ❖ Pa kusamba kwa Sunnah, pangani chitsimikizo cha chifukwa chomwe munthu akufunira kusamba. Mwachitsanzo, pangani chitsimikizo cha kusamba kwa Jumu'ah motere: ‘نَوْيِثُ النُّسُلَ لِلْجُمُعَةِ’ (Ndikupanga chitsimikizo cha kusamba kwa sunnah chifukwa cha Jumu'ah).

<sup>1</sup> al-Majmu' Sharh al-Muhazzab, vol. 3, p. 152

<sup>2</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 132

<sup>3</sup> Fath al-Mu'een, pp. 69-70, terpilih

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

- ❖ Ndi Sunnah kusamba pambuyo pochira ku misala ndi khunyu, koma chitsimikizo chopangidwa chikhale cha kusamba kokakamizika (fardh ghusl) popeza nthawi zambiri wamisala ndi wokomoka amatulutsa umuna.<sup>1</sup>
- ❖ Zili za chikakamizo kuti chitsimikizo chikhalepo panthawi yosambisa chiwalo choyamba cha thupi.
- ❖ Ngati chitsimikizo chinapangidwa pambuyo posambitsa mbali ina ya thupi, ndiyе kuti ndichikakamizo kusambitsanso chiwalocho pambuyo poti chitsimikizo chapangidwa pa kusamba kokakamizika.<sup>2</sup>

## 2. Kuthira madzi thupi lonse

Zili zofunika kuti madzi aziyenda m'ziwalo zonse za thupi kuchokera kutsitsi la m'mutu mpaka zidendene za mapazi. Izi kuphatikizapo cheya cha pathupi komanso malo omwe ali pansi pa zikhadabo. Pokhala ndi lingaliro lalikulu kuti madzi ayenderera pa thupi lonse, zimawoneka motsogolera bwino kuti kusamba kwakhala kotheka kwa thunthu. Komabe, ndi Sunnah ku onetsetsa kuti madzi akuyenderera m'makutu, m'khwapa, pa mchombo ndi mbali zonse za thupi zimene zili ndi magawo ena okwinyika.<sup>3</sup>

صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ      صَلَوَاتُ اللَّهِ عَلَى الْحَبِيبِ

---

<sup>1</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 135

<sup>2</sup> I'aanat al-Talibin, pp. 128-129/1

<sup>3</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 128

## Machenjezo 20 kwa amuna ndi akazi panthawi ya kusamba

- ❖ Ngati pali chinthu chonga uwimbo pa chiwalo china chilichonse chomwe chikulepheretsa madzi kufika pakhungu, ndikofunikira kuti chichotsedwe ndikupangitsa kuti madzi ayende pachiwalocho.
- ❖ Ngati tsitsi la munthu lili lolukidwa, ndipo madzi sakudutsa m'menemo popanda kumasula tsitsilo, ndi fardh kulimasula kuti mupite madzi. Ngati madzi angathe kudutsa popanda kulimasula tsitsilo, ndiye kuti sikuli koyenera kulimasula.
- ❖ Sikoyenera kutsuka gawo la m'kati la tsitsi lomwe lalukana mwa ilo lokha.
- ❖ Ndikoyenera kutsuka mbali zonse za khutu ndi chilichonse chomwe chikuwonekera pa bowo<sup>1</sup> la khutu.
- ❖ Malo omwe ali pansi pa khungu lomwe limadulidwa panthawi ya mdulidwe amatengedwa kuti ndi mbali ya thupi lowonekera. Choncho amene sanadulidwe asambisenso m'kati mwake mwakhungulo. Ngati izi sizingatheke, ndikofunikira (wajib) kuchita mdulidwe. Kuonjezera apo, ngati m'kati mwa khungu silikutsukidwa pambuyo pokodza ndipo gawo lapamwamba lokha

---

<sup>1</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 2, p. 122

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

ndilosambitsidwa, swalah sidzakhala yovomerezeka<sup>2</sup> kwa munthuyu.<sup>1</sup>

- ❖ Ngati mabowo a mphuno kapena makutu obooledwa sanatsekedwe, madzi ayenera kudutsamonso mmenemo.
- ❖ Tsitsi lililonse la mzikope, masharubu ndi ndevu ziyenera kusambitsidwa kuyambira momerera kufikira kunsonga, ndiponso khungu pansi pake lisambitsidwenso.
- ❖ Kwezani tsitsi kumbuyo kwa makutu ndikutsanulira madzi pamalopo.
- ❖ Kwezani mutu wanu ndikusambsa malo pakati pa chibwano ndi kholinga
- ❖ Sambitsani gawo lililonse lakumbuyo.
- ❖ Kwezani makwinya a mimba kuti muvisambitse bwino.
- ❖ Thirani madzi mu nchombo. Ngati mukukayikira kuti mchombowo sunasambitsidwe bwino, lowetsani chala m'kati mwake ndi kuusambsa.
- ❖ Tsukani tsitsi lililonse la thupi kuchokera momerera mwake mpaka kunsonga.
- ❖ Sambitsani malo wopindika pakati pa ntchafu ndi malo omwe ali pansi pa mchombo.

---

<sup>1</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 129

- ❖ Ngati mukusamba mutakhala pansi, kumbukirani kusambitsa pakati pa ntchafu ndi katumba.
- ❖ Onetsetsani kuti malo omwe ali pakati pa matako awiri asambitsidwa, makamaka pamene mukusamba muta ima.
- ❖ Thirani madzi kumbali zonse za ntchafu.
- ❖ Thirani madzi kumbali zonse za katumba.
- ❖ Thirani madzi kunsi kwa chida cha abambo ndi mazira a abambo mpaka kumapeto.
- ❖ Thirani madzi kunsi kwa mazira a abambo mpaka pamene athera.

### Machenjezo anayi kwa akazi

- ❖ Chiwalo chilichonse chamalo obisika amzimayi chomwe chimawonekera pamene wagwada chiyenera kusambitsidwa moyenera.<sup>1</sup>
- ❖ Kwezerani mabere akugwa ndikuthira madzi kunsi kwake.
- ❖ Sambitsani mzere pamalo pamene mimba ndi mawere zimakumana.
- ❖ Ndikofunikira kuchotsa zopaka (polishi) za mzikhadabo, apo ayi (ghusl) kusamba kudzakhala kosavomerezeka.

---

<sup>1</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, pp. 129.134

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

Mosiyana ndi zimenezi, palibe vuto mzopaka za mtundu wa henna.

### **Malamulo okhudzana ndi bala lomangidwa**

1. Ngati bandeji lakulungidwa pabala kapena mbali yomwe yakhudzidwa ndipo cuti kutsegula bandejilo kungayambitse vuto, ndiye cuti zinthu zitatu zili zofunika (*wajib*): Kuchita tayammamu, kusambisa chiwalo chopanda chilondacho, ndi kupukuta bandejilo ndi madzi. Komabe, ngati bandejilo lili pabalapo kapena pamalo omwe akhudzidwa, osati pamalo osavulala konse, kapena ngati malo wobisika wosavulala pansi pa bandeji, asambitsidwa mbali ina, ndiye cuti sikoyenera (*wajib*) kupukuta pamwamba pa bandejilo ndi madzi.
2. Ngati palibe vuto potsegula bandejilo ndipo malo ovulala kapena okhudzikawo akhoza kusambitsidwa, kapena pansi pa bandeji pali malo opanda mabala, kapena malo omangidwa bandejiwo ndi chiwalo mwa ziwalo zopukutidwa pa tayammamu ndipo cuti dothi lingagwiritsidwe ntchito kupukuta pamwamba pake; ndiye cuti muzochitika zonzezi nkofunika (*wajib*) kutsegula bandeji.
3. Palibe dongosolo lokhazikitsidwa lomwe likufunika pochita tayammamu panthawi ya kusamba posambisa

malo omwe ali osavulala pathupi. Komabe, ndi bwino kuyamba kuchita tayammamu.

4. Ngati bandejilo lili pa ziwalo zomwe zimapukutidwa pa nthawi ya tayammamu, kapena lakuta malo ambiri osavulazidwa kuposa momwe limafunikira, kapena yangokwirira zomwe ziyenera kuchitidwa koma inagwirtsidwa ntchito panthawi yomwe munthu anali wodetsedwa (hadath), ndiye kuti munthawi zonsenzi pafunikanso kubwereza swalah.<sup>1</sup>
5. Momwemonso, ngati pansi pa bandejilo pali zodetsedwa zomwe palibe kuchitira mwina ndiye kuti Swalah ibwerezedwanso pankhaniyi. Izi zili choncho chifukwa nkofunika kuchita qadha ya Swalah yomwe inachitika munthu ali ndi nyansi<sup>2</sup> zotere (pathupi lake).<sup>2</sup>

### **Zifukwa zisanu zopangitsa kusamba (ghusl) kukhala (fardh) chikakamizo**

1. Kutulutsa umuna
2. Ngati mutu wa chida cha abambo walowa mu maliseche amkazi mosasamala kanthu kuti izi zichitika chifukwa cha chilakolako kapena ayi komanso ngati kutulutsa umuna

---

<sup>1</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, pp. 129-130

<sup>2</sup> Haashiyah Safwah al-Zubad, vol. 1, p. 249

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

kwachitika kapena ayi; onse awiri adzayenera kusamba kokakamizika.

3. Pambuyo pa kutha kwa msambo (*haydh*).
4. Pambuyo pa kutha kwa magazi obwera kaamba kobereka (*nifaas*).
5. Kubadwa kwa mwana.<sup>1</sup>

### **Kufotokoza kofunikira kokhudza magazi pambuyo pobereka**

Akazi ambiri amakhala ndi malingaliro akuti mkazi amatengedwa kukhala wodetsedwa pambuyo pobereka kwa nyengo yotsimikizika ya masiku 40; izi sizolondola. Chonde werengani kufotokozeraku pankhani ya kutuluka kwa magazi pambuyo pobereka. Kutaya kwa magazi kumene kumachitika mwana akabadwa komanso masiku 15 asanadutse kumatchedwa kuti *nifaas*. Kutilika kwake kochepa ndi nthawi imodzi, ngakhale kuti nthawi zambiri zimatenga masiku 40. Kutilika kwa nthawiyi ndi masiku 60 kuchokera pa kubadwa kwa mwana (kutanthauza kuti, ngati magazi akupitirirabe kutuluka ngakhale patatha masiku 60, magaziwo amatengedwa ngati matenda. Choncho, amayi ayenera kusamba kokakamizika pamene atha masiku 60. Ngati magazi asiya kutuluka pasanathe masiku 60, ngakhale zitachitika kanthawi

---

<sup>1</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, 101

pang'ono pambuyo pa nthawi yobereka, mayiyo asambe pambuyo posiya kutuluka magazi ndikuyamba kuswali ndi kusala).

Ngati magazi atuluka patatha masiku 15 kuchokera pa nthawi ya kubadwa kwa mwana, izi sizidzatengedwa ngati kutuluka kwa magazi pambuyo pobereka, koma zidzayesedwa kuti ndi msambo.<sup>1</sup>

### Malamulo Atatu Ofunika

1. Kutuluka kwa umuna kumapangitsa kuti kusamba kukhale kokakamizika, mosasamala kanthu kuti umuna unatuluka chifukwa cha chilakolako kapena ayi, panthawi yogona kapena kukhala maso, pang'ono kapena mochuluka, ngakhale chifukwa cha matenda. Nthawi zonzezi kusamba kuli fardh.
2. Ngati kudzilotera kwachitika koma umuna sunawoneke kapena pali chikaiko cha kutuluka kwa umuna, kusamba Sikuli kofunikira (*wajib*). Ngati umuna unawoneka koma osakumbukira za kutulutsa kwa kudzilotera, kusamba kudzakhala kofunikira.
3. Kutulutsa umuna poseweretsa maliseche kumapangitsa kuti kusamba kukhale kokakamizika. Ndipo ndi tchimo

---

<sup>1</sup> Nihayah al-Muhtaj, vol. 1, p. 202

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

kutero.<sup>1</sup> (Mchitidwe wamanyaziwu) umabweretsa kusowa mphamvu<sup>2</sup> zamunthu wamamuna, ndipo zawonedwa kawirikawiri kuti munthu woteroyo amakhala wosakwatira.

### Chilango chodziseweretsa maliseche

Imam Ahmad Raza Khan al-Hanafi رحمۃ اللہ علیہ anafunsidwa funso ili: “Pali majluq (wodziseweretsa maliseche) amene sasiya kuchita zamanyazizi ngakhale akulangizidwa. Kodi adzaukitsidwa motani? Kodi ndi pemphero liti limene angapemphe kuti asiye chizolowezi chimenechi?”

Imam Ahmad Raza Khan رحمۃ اللہ علیہ anayankha kuti: “Iye ndi wochimwa, wosamvera<sup>3</sup>, wolakwa pakuchita tchimo lalikulu (chifukwa cholimbikira) ndi wopyola malire. Patsiku lachiweruzo, manja a anthu oterowo (odziseweretsa maliseche) adzaukitsidwa ali ndi pathupi, ndipo adzayalutsidwa pamaso pa msonkhano waukulu wa anthu ngati sakulapa. Allah عَزَّوجَلَّ Wamphanvu zonse amakhululukira amene wamfuna ndipo amamulanga amene wamfuna. Munthu woteroyo ayenera kuwerenga ”لَا حَوْلَ وَلَا قُوَّةَ إِلَّا بِإِنْشَاءِ اللَّهِ الْعَظِيمِ“ mochuluka, ndipo Satana akamuyesa kuti adziseweretsa maliseche, nthawi yomweyo

---

<sup>1</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, pp. 122-127

<sup>2</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 130

<sup>3</sup> Mukafuna zambiri zokhudza zowopsa za kudziseweretsa maliseche, werengani Buku la Ameer Ahlus Sunnah lotchedwa ‘Amrad Prasand ki Tabakariya’.

atembukire kwa Allah ndikuwerenga “**لَا حَوْلَ وَلَا قُوَّةَ إِلَّا بِاللَّهِ الْعَلِيِّ**”<sup>1</sup> kuchokera pansi pa mtima wake. Ayenera kupemphera Swalah zisanu tsiku lililonse nthawi zone. Pambuyo pa Swalah ya Fajr, akuyenera kuwerenga Surah al-Ikhlaṣ pafupi pafupi. ”**وَاللَّهُ أَعْلَمُ**”

(Kwalembewa patsamba 16 la *Shajarah Atṭariyyah* kuti ngati munthu awerenga Surah al-Ikhlaṣ kokwana ka 11 m'mawa uliwonse, satana pamodzi ndi magulu ake onse ankhondo sangapambane pomupangitsa munthu woteroyo kuchimwa pokhapokha iye mwini atachimwa.)

### Ndi nthawi iti pamene kusamba kuli Sunnah?

- ❖ Jumu'ah.
- ❖ Eid al-Fitr.
- ❖ Eid al-Adha.
- ❖ Mapemphero a kadamsana wa Dzuwa ndi mwezi (Swalah ya Kusuf ndi Swalah ya Khusuf).
- ❖ Swalah ya mvula (Swalah al-Istisqa).
- ❖ Asanavale ihram.
- ❖ Kuyimirira pa Arafat.

---

<sup>1</sup> Fatawa Razawiyyah, vol. 22, p. 244

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

- ❖ Kuyimirira pa Muzdalifah.
- ❖ Asanayambe kuchita azan.
- ❖ Asanalowe al-Haramayn al-Sharifayn ndi mzikiti uliwonse.
- ❖ Asanagende zipirara m'masiku atatu a Ayyaam al-Tashreeq (Si Sunnah kusamba asanagende Jamarah Aqabah popeza izi zili zapafupi kusamba komwe kumachitika pa nthawi yokhala (*wuqoof*) pa Muzdalifah).
- ❖ Pambuyo posambitsa wakufa.
- ❖ Kupanga itikafu mu mzikiti.
- ❖ Usiku uliwonse wa Ramadhan.
- ❖ Msonkhano wamadalitso usanachitike, monga misonkhano yankhani zachipembedzo, zikr, kuphunzira ndi kuphunzitsa za Chisilamu.
- ❖ Pambuyo pa kuchotsa magazi (*hijamah*).
- ❖ Kuchotsa fungo loipa la pathupi.
- ❖ Kwa munthu wamisala amene wachira.
- ❖ Munthu wokomoka akatsitsimuka ngati sakutuluka umuna, apo ayi kudzakhala kokakamizika kusamba.
- ❖ Mwana akatha msinkhu chifukwa cha zaka.
- ❖ Kumeta tsitsi lakumalo obisika.

- ❖ Kuchotsa tsitsi lakukhwapa.
- ❖ Ndi Sunnah kwa kafiri kusamba pambuyo polowa Chisilamu ngati kusamba sikunali kokakamizika pa nthawi ya ukafiri. Apo ayi, padzakhala mitundu iwiri ya kusamba: kusamba kwa Sunnah komanso kusamba kwa fardh.
- ❖ Kuchokera mu zonsezi, kusamba komwe kuli kotsindika kwambiri ndi kwa Jumuah kotsatiridwa ndi kusamba pambuyo posambitsa maliro<sup>1</sup>

### **Zitsimikizo zingapo mukusamba kumodzi**

Ngati wina wafuna kusamba kwa fardh-kuti ayeretsedwe pambuyo pa chonyansa chachikulu mwachitsanzo (*janabah*) - komanso anafuna kuchita kusamba kwa Sunnah - mwachitsanzo pa Jumu'ah, - zitsimikizo ziwirizi mukusamba kumodzi zidzapangitsa kupeza (ubwino) wa zitsimikizo zonse ziwiri. Komabe, ndibwino kuziyeretsa posamba kulikonse pawokha pawokha poyamba kusamba poziyeretsa kuchokera ku zonyansa zazikulu, kenako ndikusamba kwa Sunnah ya pa Jumu'ah.

Ngati kusamba kwachitidwa ndi cholingga cha kusamba kwa fard kapena kusamba kwa Sunnah, ndiye kuti kusamba kokhako komwe kwapangidwa motsimikiza kudzakhala kokwanira.

---

<sup>1</sup> Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, pp. 428-429; I'aanat al-Talibeen vol. 2, pp. 122-124

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

- ❖ Ngati kusamba kwa ma Fardh angapo ali oyenera kuti munthu wina akwaniritse, kuchita chitsimikizo chofuna kukwaniritsa kusamba kumodzi, kudzapangitsa kukwaniritsidwa kusamba konse. Mwachitsanzo, mkazi amene ayenera kusamba kokakamizika chifukwa cha m'sambo komanso kupeza chiyero kuchokera ku chidetso chachikulu, akhoza Kuyika chitsimikizo chosambira chimodzi mwa izi ndipo chinacho chidzakwaniritsidwa. Momwemonso ngati pali kusamba kungapo kwa ma Sunnah, kupanga chitsimikizo chimodzi mwa izo kudzapangitsa kuti enanso akwaniritsidwe. Mwachitsanzo, kusamba kwa Sunnah ya pa Eid, Jumuah ndi kadamsana wa dzuwa.<sup>1</sup>

### Kusamba pamvula

Ndi zoletsedwa kusamba pamaso pa anthu powonetsa malo obisika<sup>2</sup>. Ngati mukusamba pamvula, valani nsalu yokhuthara kwambiri, yamtundu pamwamba pa Buluku kapena mtocha. Mwanjira iyi, ngakhale zovalazo zitanyowa ndikumamatira ku thupi, mtundu wa ntchafu zanu ndi ziwalo zina siudzaonekera.

---

<sup>1</sup> Fath al-Jawad, vol. 1, p. 92

<sup>2</sup> Sharh Muslim lil-Nawawi, vol. 2, p. 37

**Malamulo asanu ndi anayi okhudzana ndi kuwerenga kapena kukhudza Quran Yopatulika munthu ali ndi unwe wa ukulu**

1. Amene alibe wudhu kapena sanasambe [panthawi yake] sangathe kuswali, kuchita tawaf, kuchita sajidah yowerengera Quran (sajdah al-tilawah) kapena sajidah yothokoza (sajdah al-shukr). Momwemonso, sakuyenera kugwira Quran yopatulika, kukhudza chikuto chake kapena masamba (mapepala) ake, ndikugwira kapena kukhudza chikwama kapena bokosi lomwe lili ndi Quran Yopatulika lomwe linapangidwira ndi cholinga chosungiramo Quran. Kugwira kapena kunyamula chilichonse chomwe chalembedwa gawo la ndime ya Quran ndi cholinga chofuna kuphunzitsa kapena kuwerenga, kulinso koletsedwa.<sup>1</sup>
2. Ndi koletsedwa kwa munthu amene kusamba ndikokakamizika kwa iye kukhala mu Mzikiti. Zili chimodzimodzi kwa iye sakuyenera kuwerenga Quran Yopatulika ngakhale kuti sanayigwire ngakhale itakhala gawo chabe ya vesi.<sup>2</sup> Komabe zikuloledwa kwa munthu wotero kuyang'ana Quran Yopatulika ndikuiwerenga m'maganizo chabe popanda kusuntha lilime.<sup>3</sup>

---

<sup>1</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, pp. 113-115

<sup>2</sup> Fath al-Mu'een, p. 64

<sup>3</sup> Al-Majmu' Sharh al-Muhazzab, vol. 3, p. 125

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

3. Sizili zoletsedwa [kwa munthu wofunika kusamba kokakamizika] kuwerenga Quran Yopatulika ndi cholinga chochita ma zikr, kuchita *du'a* kapena kulandira madalitso (*tabarruk*), malingana ngati cholinga sichinali kuwerenga Quran Yopatulika. Mwachitsanzo, kuwerenga بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ pamene mukudya سُبْحَانَ اللَّهِ يَعْلَمُ مَا فِي الْأَرْضِ pamene mwamaliza kudya سُبْحَانَ رَبِّ الْجِنْوَنِ pamene mukukwera chokwera إِنَّ اللَّهَ وَإِنَّا لِإِلَيْهِ سَاجِدُونَ pamene vuto lililonse lagwa.<sup>1</sup>
4. Momwemonso, ngati wina awerenga Quran Yopatulika popanda cholinga choyiwerengera kapena cholinga china chilichonse, izinso sizoletsedwa.<sup>2</sup>
5. Ndi zoletsedwa kugwira Quran Yopatulika kapena imodzi mwa ma vesi ake popanda wudhu.<sup>3</sup> Kuwerenga Quran Yopatulika (poikumbukira mmunu kapena kuyang'ana) koma popanda kuigwira, zili zololedwa, koma kulibwino kuchita wudhu ndikuyiwerenga.<sup>4</sup>
6. Munthu amene alibe wudhu kapena amene ayenera kusamba kwachikakamizo atha kulemba Quran Yopatulika

---

<sup>1</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 120; Nihayah al-Muhtaj, vol. 1, p. 133

<sup>2</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 120

<sup>3</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 113

<sup>4</sup> al-Majmu' Sharh al-Muhazzab, vol. 3, p. 126

popanda kugwira kapena kukhudza pepala kapena sileti yomwe ikulembedwayo<sup>1</sup>.

7. Ndi zoletsedwa kumeza chilichonse (monga pepala) cholembedwapo Quran Yopatulika kapena dzina la Allah. Komabe zidzakhala zololedwa kutero, ngati zidyedwa m'njira yochitsa kuti zolembazo zikhale zitasedewa bwino zisanafike m'mimba<sup>2</sup>.
8. Kulemba ndime kapena vesi ya mu Quran yoyela pa mbale ndicholina chopeza machilitso pakumwa madzi kuchokera mbalemo ndizololedwa.<sup>2</sup>
9. Nzonyansa (makruh) kwa munthu amene kusamba Sikulikokakamizika kwa iye koma pakamwa pake padetsedwa kuwerenga Quran Yopatulika..<sup>3</sup>

### **Kugwira mabuku achipembedzo opanda wudhu**

Ndi zololedwa kwa munthu amene kusamba ndikokakamizika kapena amene alibe wudhu kugwira kapena kukhudza mabuku ama Hadith, fiqh, usool, ndi ena otero. Komabe, ndibwino kukhala oyeretsedwa munthu asanagwire kapena kunyamula mabuku ama Hadith<sup>5</sup>.

---

<sup>1</sup> Tuhfah al-Muhtaj ma Haashiyah Sharwani, vol. 1, p. 155

<sup>2</sup> Mughni al-Muhtaj, vol. 1, p. 125

<sup>3</sup> al-Majmu' Sharh al-Muhazzab, Kitab al-Taharah, vol. 3, p. 126

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

## Kufunira mtendere ndi madalitso (salat) kwa Mtumiki okondedwa pamene munthuyu ali mu umve

سُبْحَنَ اللَّهُ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ، أَكْبَرُ، الْحَمْدُ لِلَّهِ،  
Ndizololedwa kuwerenga kwa munthu yemwe kusamba kuli kokakamizika kwa iye, kumfunira *zabwino* Mtumiki ndi kuchita ma du'a ena. Ndizololedwanso kuyankha azan<sup>2</sup> ikamachitika.

## Kodi ndi nthawi iti yomwe mwana amakhala wamkulu?

Pamene anyamata ndi atsikana ali ndi zaka pafupifupi zisanu ndi zinayi (kutengera kalendala ya Hijri) ndipo zizindikiro za kutha msinkhu zikuwonekera, amatengedwa ngati akuluakulu. Makamaka, mnyamata kapena mtsikana akatulutsa umuna ali m'maso kapena ali m'tulo, kapena mtsikana wayamba kuwona msambo, adzaganiziridwa kuti watha msinkhu. Ngati kutulutsa umuna kwachitika masiku 15 asanakwanitse zaka zisanu ndi zinayi, adzaganiziridwanso kuti watha msinkhu. Ngati zotuluka zitachitika kwa masiku 16 kapena kuposera apo pamene asanakwanitse zaka zisanu ndi zinayi, kutulutsako sikungatengedwe ngati umuna, ndipo mnyamatayo sadzawerengedwa kuti ndi wamkulu malingana ndi shariah. chimodzimodzi, ngati mtsikana ataya magazi kwa masiku 16 kapena kuposera apo koma sanakwanitse zaka zisanu ndi zinayi, izi sizingaonedwe ngati msambo, ndipo mtsikanayo sadzawerengedwa kuti ndi wamkulu malingana ndi shariah. Ngati palibe chizindikiro cha kutha msinkhu, mwanayo

adzalingaliridwa kukhala kuti watha msinkhu ndikukhala munthu wamkulu akafika zaka 15.<sup>1</sup>

Ndevu za mnyamata kapena masharubu zikayamba kukula, kapena kuti bele la mtsikana likayamba kukula sizizindikiro za kukula kwake.<sup>2</sup>

### **Kodi mabuku ayenera kusungidwa mu ndondomeko yotani?**

1. Quran Yopatulika iyenera kusungidwa pamwamba pa mabuku ena onse, kenako Sahih al-Bukhari, kutsatiridwa ndi Sahih Muslim, kenako mabuku ena a Sahih Hadith. Pambuyo pake payenera kukhala mabuku a kufotokozerwa Quran (tafseer), kufotokoza kwa (sharh) ma Hadith, mfundo (usool) zachipembedzo, mfundo za fiqh, ndipo potsiriza, mabuku a fiqh. Ngati pali mabuku awiri amtundu umodzi, ndiye kuti buku lomwe lili ndi zambiri za Quran Yopatulika liyikidwe pamwamba pake, kenako buku lomwe lili ndi ma Hadith ochulukirapo, kenako la wolemba wolemekezeka kwambiri, kenako mabuku a olemba akale kwambiri, kenako mabuku omwe ali m'manja mwa akatswiri a maphunziro ndi olungama kwambiri, kenako mabuku owona kwambiri. Ndi bwino

---

<sup>1</sup> Nihayah al-Muhtaj, vol. 3, p. 295

<sup>2</sup> Fatwa Haditsiyah, p. 403

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

mbali yotsegulira mabuku kuti ikhale ikuyang'ana mmwamba.<sup>1</sup>

2. Imam Abu Abdullah Husein Ibn Hassan al-Halimi al-Shafi'I رحمه الله عاليه akunena kuti: "Mbali yomulemekeza Allah ndi Mtumiki Wake صلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ ndiye kusayika Mabuku kapena katundu wa mnyumba pamwamba pa Quran Yopatulika kapena pamwamba pa mabuku a Hadith."<sup>2</sup>

### **Kuyika ndalama kapena zinthu zina mkati mwa pepala lomwe lili ndi zolemba zachipembedzo**

Ndi zosaloledwa kuika ndalama kapena china chilichonse mkati mwa pepala lomwe lili ndi Quran kapena dzina lolemekezeka monga Allah kapena Muhammad صلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ litalembedwa papepalalo.<sup>3</sup>

### **Chiyambi cha manong'onong'o a satana**

Kukoza pamalo omwe munthu amasambirapo ndimchitidwe wonyansa (makruh). Mtumiki wa Allah صلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ waletsa zimenezi ponena kuti: "Ndithu, izi nthawi zambiri zimabweretsa manong'onong'o a satana.

---

<sup>1</sup> Al-Minhaj fi Shu'ab al-Imaan, vol. 2, p. 149, Dar al-Fikr, Beirut

<sup>2</sup> Fatwa Haditsiyah,, p. 400

<sup>3</sup> Abu Dawud, p. 21, Hadits 27

Kuletsa kumeneku kumagwira ntchito ngati palibe paliponse pomwe madzi ndi mkodzo umatulukirapo (ndipo zimasonkhana pamalo amodzi). Ngati pali ngalande yomwe imapangitsa kuti madzi ndi mkodzo zidutse, ndiye kuti izi sizikuletsedwa.<sup>1</sup>

## Tayammamu

### Ntchito zokakamizika (*faraidh*) za *tayammamu*

Pali ntchito zisanu zokakamizika pa *tayammamu*:

1. Kudusitsa dothi pa ziwalo za thupi.
2. Kupanga chitsimikizo cha Swalah kapena kupanga chinthu chololedwa (*mubah*) chimene ukhondo (*twahara*) uli wofunikira, monga kugwira Quran. Kuchita tayammamu yomwe ikupereka chilolezo kupemphera Swalah ya fardh kupangitsa kuti zikhale zololedwa kugwira Quran ndi kupemphera Swalah ya fardh ndi Swalah yapadera (*nafl*).  
❖ Kupanga chitsimikizo cha Swalah yapadera (*nafl*), Swalah iliyonse, Swalah ya maliro kapena ulaliki (*khutbah*) wa Jumuah kumapangitsa chilichonse kukhala chololedwa kupatula chomwe chili chochita munthu payekha (*fardh ayn*).

---

<sup>1</sup> Mughni al-Muhtaj, vol. 1, p. 136

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

- ❖ Nkosaloledwa kupemphera Swalah iliyonse ngati tayammamu yachitidwa ndi cholinga china osati cha Swalah, monga kugwira Quran. Komabe, china chilichonse chikhala chooledwa.
  - ❖ Zili Fardh kusunga chitsimikizo m'maganizo mwanu kuyambira pomwe dothi latengedwa kufikira kupukuta ku nkhopo kwayambika.
3. Kupukuta nkhopo yonse.
  4. Kupukuta manja mpaka ndi kuphatikiza zigongono.
  5. Kusunga ndondomeko popukuta nkhopo poyamba, kenako mikono.<sup>1</sup>

### Zochita 19 za ma Sunnah pa tayammamu

1. Kuwerenga ﷺ musanayambe kuchita tayammamu.
2. Kuyang'ana ku qiblah.
3. Kugwiritsa ntchito miswak.
4. Kwa munthu wovala mphete, ayenera kuyichotsa asanamenyetse manja ake padothi koyamba (kuti nkhopo ipukutidwe ndi manja onse, ndipo ndikofunikira [wajib]

---

<sup>1</sup> Al-Manhaj al-Qawim, p. 138, ringkasan

kuchotsa mphete pomenyetsa manja (padothi) kachiwiri ndicholinga chakuti dothi lifikire mbali zonse za manja).

5. Kutambasula zala pamene mukumenyetsa manja padothi nthawi zonse ziwiri.<sup>1</sup>
6. Kumenyetsa manja onse awiri padothi nthawi imodzi.<sup>2</sup>
7. Kusisita m'manja kapena kuuzira dothi lomwe lili lochulukirapo mpakana patatsala fumbi lomwe likufunika (m'manja).
8. Kuyamba kupukuta nkhopre kuchokera pamwamba.
9. Kuyamba kupukuta dzanja lamanja, kenako lamanzere.
10. Kupukuta zikhatho zonse ziwiri.<sup>3</sup>
11. Kupukuta manja kuchokera pakasukusuku mpakana paphewa.<sup>4</sup>
12. Kuchita *khilal* zala za manja onse awiri.
13. Osakweza manja kuchokera kumaso kapena m'mikono mpaka onse atapukutidwa mokwanira.<sup>5</sup>

---

<sup>1</sup> Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, pp. 163.164, terpilih

<sup>2</sup> Fath al-Jawad, vol. 1, p. 112

<sup>3</sup> Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, p. 164

<sup>4</sup> al-Manhaj al-Qaweem, p. 139

<sup>5</sup> Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, p. 163

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

14. Kuyendetsa manja pankhope kumanso m'mikono monga momwe zimachitira pa wudhu.
15. Osabwerezza kupukuta.<sup>1</sup>
16. Kuchita *tayammamu* popanda kuyimitsa.<sup>2</sup>
17. Kupanga zikr ndi kupanga du'a pambuyo pa *tayammamu* monga momwe zimachitikira pambuyo pa wudhu.<sup>3</sup>
18. Kuchotsa dothi mziwalo zomwe zinapukutidwa pa nthawi ya *tayammamu* pambuyo pomaliza Swalah.<sup>4</sup>
19. Kupemphera ma (rakah) awiri a Swalah pambuyo pa *tayammamu*<sup>5</sup>

### Njira za *Tayammamu* (Shafi'i)

Yang'anani ku Qiblah, nenani بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ ndikugwiritsa ntchito miswak. Kenako pangani chitsimikizo chochita *tayammamu* chitsimikizo chimenechi chikhoza kupangidwa motere: "Ndikuchita *tayammam* kuti kupemphera Swalah ya Fardh kukhale kololedwa." Pokhala ndi chitsimikizo ichi m'maganizo mwanu, menyetsani manja anu pa dothi zala zanu

---

<sup>1</sup> Al-Manhaj al-Qaweem, p. 139

<sup>2</sup> Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, p. 164

<sup>3</sup> Haashiyah al-Tarmasi ala al-Manhaj al-Qaweem, vol.2, p. 261

<sup>4</sup> Tuhfah al Muhtaj, vol. 1, p. 164

<sup>5</sup> Fatwa al-Ramli, vol. 1, p. 57

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

zili zotambasula. Ngati dothi lachuluka m'manja, lichotseni posasa manja kapena kuliwuzira (ndi mpweya).

Pukutani manja pankhope yonse osasiya mbali imodzi. Pukutaninso nsonga yakutsogolo ya mphuno ndi mbali ya ndevu zomwe zikuzendewera kumaso. Zili fardh kuditiriza chitsimikizo m'maganizo mpakana mutayamba kupukuta kunkhope.

Momwemonso monga kale, menyetsani manja anu padothi ndi kupukuta mikono kuchokera ku zikhadabo mpakana ku kasukusuku. Ndi Sunnah kupukuta manja mpakana m'mapewa. Njira yodziwika bwino yopukutira manja ndikuyamba kuyika mbali ya m'kati ya zala zinayi za dzanja lamanzere (kupatula chala chachikulu) kumbuyo kwa zala za dzanja lamanzere. Kenako, pukutani mpakana mmalungiro a dzanja. Kenako, kulungani zala za dzanja lamanzere kuzungulira mmalungiro a dzanja, ndi kuzikwezeka kufikira m'kasukusuku.

Zikatha izi, chala chachikulu chili chokwezekabe, gwiritsani ntchito chikhatho chamanzere kuti mupukute mbali yamkati ya chikhatho chakumanja mpaka kufikira mmalungiro a dzanja. Tsopano, gwiritsani ntchito gawo la m'kati la chala chakumanzere kupukuta kumbuyo kwa chala chakumanja. Gwiritsani ntchito dzanja lamanzere kupukuta dzanja lamanzere chimodzimodzi. Pambuyo pake, zikhatho za manja onse awiri

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

zimapukutidwa pamodzi, ndipo *khilal* imachitidwa pa zala za manja<sup>1</sup> onse awiri.<sup>1</sup>

### **Ngale 25 za Madani zokhudzana ndi Tayammamu**

1. *Tayammamu* ndiyololedwa kuchita ndi dothi lililonse lomwe lili ndi fumbi. Dothi lonyowa lomwe lilibe fumbi silingagwiritsidwe ntchito pa *tayammamu*.
2. Kugwiritsa ntchito dothi lomwe lalandidwa molakwika kapena lomwe lili la mziki ndi zoletsedwa. Komabe, ngati litagwiritsidwa ntchito, *tayammamu* ndiyovomerezeka.<sup>2</sup>
3. Kupatula dothi, zinthu zina monga miyala ya layimu ndi za ufa sizingagwiritsidwe ntchito popanga *Tayammamu*.<sup>3</sup>
4. Dothi losakanizidwa ndi zinthu monga ufa, layimu ndi safironi silingagwiritsidwe ntchito pa *tayammamu*.
5. Ndikofunikira kuti dothi logwiritsidwa ntchito pa *tayammamu* likhale loyera (lopanda nyansi.)
6. Ndizosaloledwa kuchita *tayammamu* ndi dothi lonyansa. Mwachitsanzo, *tayammamu* singapangidwe pogwiritsa ntchito dothi losakanizidwa ndi mkodzo kenako n'kuumitsa, kapena

---

<sup>1</sup> Al-Majmu' Sharh al-Muhazzab, vol. 3, p. 207

<sup>2</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 100

<sup>3</sup> Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, p. 158

ndowe za ng'ombe zomwe zinanyenyeka n'kusakanizika ndi dothi.<sup>1</sup>

7. Ndi zololedwa kugwiritsa ntchito fumbi la pa pilo, zovala, mphasa kapena khoma pochita *tayammamu*<sup>2</sup>
8. Ngati madzi sangagwiritsidwe ntchito ndi munthu yemwe alibe wudhu kapena woti kusamba ndikokakamizika, *tayammamu* ikhoza kuchitika m'malo mwa wudhu komanso kusamba.<sup>3</sup>
9. Ngati pogwiritsa ntchito madzi pali mantha odwalitsa, matenda kupitabe patsogolo, kutaya moyo, kutaya chiwalo kapena chiwalo kusiya kugwira ntchito yake, kuchedwa kuchira ndi kukhala bwino kapena chilema chowonekera chokha pa thupi (khungu), *tayammamu* ikhoza kuchitidwa mmalo mwake.<sup>4</sup>
10. Ngati munthu sakutha kupeza madzi kapena kuwapeza pa mtengo wokwera kuposa mtengo wanthewi zonse, *tayammamu* ikhoza kuchitidwa m'malo mwake.<sup>5</sup>
11. Munthu ayambe wafunafuna madzi kumene angayembekezere kuwapeza, monga m'nyumba mwake,

---

<sup>1</sup> Tuhfah al Muhtaj, vol. 1, pp. 158-159

<sup>2</sup> Al-Majmu' Sharh al-Muhazzab, vol. 3, p. 198

<sup>3</sup> Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, p. 148

<sup>4</sup> Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, p. 154

<sup>5</sup> I'aanat al-Talibin, vol. 1, p. 99

pakati pa katundu wake kapena kuwafunafuna kwa anzake. Ngati sakupenezeka ndipo wina ali pa nthaka, akuyenera kufunidwa mbali zonse zinayi mtunda wotalika mayadi 300 kapena 400 (*hadd ghawth*). Ngati nthaka siili yofanana, munthu ayenera kupita pa malo okwera apafupi ndi kukafufuza pamtunda wangati womwewo. Ngati madzi sakupenezeka, ndiye kuti *tayammamu* iyenera kuchitidwa.

12. Ngati pali kuthekera kuti madzi angapezeke m'kati mwa theka la kilomita (*hadd qurb*: pafupifupi mailosi imodzi ndi theka), ndizokakamizika (*wajib*) kupeza madziwo. Ngati mtunda opitirira apo, *tayammamu* ikhoza kuchitidwa.
13. Ngati munthu wina wopanda wudhu kapena amene ayenera kusamba kokakamizika atapeza madzi osakwanira kuziyeretsera, omwe alipowo ayambe kugwiritsira ntchito, kenako *tayammamu* iyenera kuchitidwa ku ziwalo zotsalira za thupi.<sup>1</sup>
14. Ngati madzi kapena dothi palibe, monga m'chipululu chokhala ndi miyala ndi mchenga wokha, Swalah ya fardh nthawiyo iyenera kupempheredwa kenako kubwerezedwa pambuyo pake. Zidzakhala zosaloledwa kwa munthu woteroyo kupemphera Swalah yodzipereka (*nafl*) kapena Swalah yophonyedwa (qadha) kapena kugwira Quran Yopatulika. Ndipo ngati kusamba kuli

---

<sup>1</sup> Al-Manhaj al-Qaweem, pp. 128-129

kokakamizika kwa munthu woteroyo, nkoletsedwa kwa iye kukhala mu Nzikit kapena kuwerenga (kupanga *qiraah*) kuposa Surah al-Fatiha mu Swalah ya fardh pa nthawiyo ndikukhalabe mu Nzikit.<sup>1</sup>

15. Ngati munthu wa pa ulendo akuopa kuti kufunafuna madzi kungamusianitse iye ndi amene akuyenda naye pawulendo kapena kuti nthawi ya Swalah ikhoza kutha, iyeyo akhoza kuswali atachita tayammamu Komabe, tayammamu siingachitidwe ndi munthu wokhala ndi madzi amene akuwopa kuti kuwagwiritsa ntchito madziwo pofuna kudziyeretsa kungafikitse nthawi ya Swalah kutha. Munthu woteroyo adzayenera kukhala oyera pogwiritsa ntchito madziwo, ngakhale nthawi ya Swalah itatha.<sup>2</sup>
16. Nkoyenera (*wajib*) munthu kubwerezanso swalah yomwe anapemphera ngati anachita *tayammamu* chifukwa cha matenda kapena bala kapena chifukwa chosapeza madzi ali pa wulendo limeneli ndi tchimo.<sup>3</sup>
17. Munthu sangachite *tayammamu* pamalo pomwe pamapezeka madzi, ngakhale atakhala kuti munthuyo akuopa kutha kwa nthawi ya Swalah pomwe akufufuza madziwo.<sup>4</sup>

---

<sup>1</sup> Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, pp. 170-171

<sup>2</sup> Al-Manhaj al-Qaweem, p. 130

<sup>3</sup> Al-Majmu' Sharh al-Muhazzab, vol. 2, p. 299

<sup>4</sup> Al-Manhaj al-Qaweem, p. 130

18. Ngati pali chitsimikizo chopeza madzi, ndibwino kudikirira ndi kuchedwerapo nthawi ya Swalah. Ngati munthu akungoganiza chabe kuti madzi apezeka kapena akukayikira, ndi bwino kuchita *tayammamu* ndi kuswali mwachangu.<sup>1</sup>
19. Munthu akhoza kuchita *tayammamu* chifukwa cha nyengo yozizira m'nthawi izi: Ngati kutenthetsa ziwalo za thupi (pambuyo pa wudhu kapena kusamba) sikukupindula, ndipo chinthu chomwe chingagwiritsidwe ntchito pofuna kutenthetsa madzi sichikupezeko. Momwemonso, zili zoyeneranso kuchita *tayammamu* ngati kugwiritsa ntchito madzi kungayambitse vuto kwa munthu, monga kusiya kugwira ntchito kwa chiwalo chathupi. Ngati mavuto amenewa sanapezeke, *tayammamu* siingachitike.<sup>2</sup> Dziwani kuti Swalah iliyonse yopempheredwa ndi *tayammamu* chifukwa cha nyengo yozizira, iyenera kubwerezedwa pambuyo<sup>3</sup> pake.
20. *Tayammamu* isanachitike, ndikofunikira kuchotsa zonyansa zilizonse m'thupi (ngati zilipo) komanso kudziwa mbali ya Qiblah (komwe kuli kofunikira).
21. Pa ntchito iliyonse ya chikakamizo yomwe munthu akuyipanga payekha (*fardh ayn*), *tayammamu* iyenera

---

<sup>1</sup> Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, p. 150

<sup>2</sup> Al-Manhaj al-Qaweem, p. 133

<sup>3</sup> Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, p. 172

kuchitidwa. Mowonjezeranso pamenepa, nkofunika kuchita *tayammamu* nthawi ya Swalah imene munthu akufuna kupemphera ikakwana.<sup>1</sup>

22. *Tayammamu* imaonongeka ndi zinthu zonse zomwe zimaononganso wudhu. Komabe pochita *tayammamu* m'malo mwa kusamba, *tayammamu* simawonongeka ndi chilichonse chimene chima wononga wudhu.<sup>2</sup>
23. Ngati munthu amene anachita *tayammamu* chifukwa chakusowa kwa madzi akuganiza kuti madzi alipo Swalah isanayambe, *tayammamuyo* idzawonongeka. Ngati pa nthawi ya Swalah madzi apezeka kapena munthu akuganiza kuti madzi alipo tsopano, *tayammamu* siidzawonongeka. Komabe, ngati madzi atapezeka pa Swalah yomwe ndi yofunika (*wajib*) kubwereza, *tayammamuyo* idza wonongeka.
24. Ngati munthu wina angachite *tayammamu* chifukwa cha matenda, *tayammamuyo* idzawonongeka ngati munthuyu atachira ku matendawo.<sup>3</sup>
25. Ngati munthu wina sangathe kuchita *tayammamu* yekha, akhoza kulola munthu wina kuti amuthandize. Pamenepa nkofunika kwa munthu amene akuchitiridwa *tayammamu*

---

<sup>1</sup> Al-Manhaj al-Qaweem, p. 137

<sup>2</sup> Haashiyah Bujayrmi ala al-Khateeb, vol. 1, p. 431,

<sup>3</sup> Tuhfah al Muhtajj, vol. 1, p. 165

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

kukhala ndi chitsimikizo chake kuyambira pomwe akutenga dothi kufikira mbali ina ya nkhopetitapukutidwa.<sup>1</sup> Kuchitiridwa *tayammamu* ndi munthu wina popanda chifukwa chomveka, ndi zinthu zonyansa (*makruh*).<sup>2</sup>

### Malangizo a Madani

Kuti muphunzire za malamulo a wudhu, werengani kabuku kamene kasindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah pamutu wakuti, *Njira ya kapangidwe ka Wudhu* (Shafi'i). Kuwonjezera apo, kuti muphunzire za Swalah, yang'anani kabuku ka *Njira ya kapempheredwe ka Swalah* (Shafi'i).

E, Allah, tipatseni luso lowerengera, kumvetsetsa ndi kufikitsa kwa ena zokhudza malamulo a kusamba nthawi zambiri. Tipatseni kuthekera kosamba molingana ndi Sunnah.

أَمِينٌ بِجَاءُهُ خَاتَمُ النَّبِيِّنَ ﷺ

### Mukamaliza kuwerenga kabukuka, perekani kwa ena mokoma mtima

Pezani mphotho Popereka timabuku ta Maktaba-tul-Madina m'misonkhano monga ma ukwati, zikumbutso zapachaka (*urs*)

---

<sup>1</sup> Tuhfah al Muhtaj, vol. 1, p. 160

<sup>2</sup> Haashiyah Sharwani ala Tuhfah al-Muhtaj, vol. 1, p. 356

Njira ya Kasambidwe {kusamba} (Shafi'i)

ndi Milad. eni sitolo ayenera kusunga timabuku timeneti m'masitolo awo ndi kupereka ngati mphatso kwa makasitomala ndi cholinga cholandira mphotho. Mwezi uliwonse, perekani mocheperako kabuku kamodzi kapena buku lolimbikitsa Sunnah lokhala ndi ngale za Madani ku nyumba za m'dera lanu. Chitani izi kuti mufalitse kuitanira mkulungama ndikupeza malipiro aakulu.

الحمد لله رب العالمين وصلوات وسلام على سيد المرسلين الذي بلغنا به نور من الشفاعة والثواب والبركات بمنه الله الرحمن الرحيم

### Kukhala msilamu woopa mulungu ndi wopemphera Salah

Khalani usiku onse mu ijtimya Dawat-e-Islam yolinbikitsa sunna yomwe imachitika lachinayi sabata iliyonse pambuyo pa salat-ul-maghrib m'dera lanu, chifukwa chomusangalatsa Allah ﷺ ndi zolina zabwino. Kuti muphunzire ma Sunnah, chipangeni kukhala chizolowez chanu choyenda ndi Madani Qafilah masiku atatu mwezi uliwoswe pamodzi ndi odzipereka a Rasool, kumalizitsa kulemba mkabuku ka Madani In'amaat tsiku lilonse kuchita fikr-e-Madina ndikupereka kwa m'bale wachisilamu woyenera yemwe ali ndi udindo mdera lanu tsiku loyamba la mwezi uliwoswe wa Madani.

#### Cholinga changa cha madani

Ndiyenera kuyesetsa kudzikonza ndekha ndi anthu apadzikio lonse lapansi، ﴿عَلَيْهِ الْكَفَلَةُ﴾. Ndicholingu choti tidzisinthe tokha, tiyenera kuchitapo kanthu pa Madani In'amaat ndikuyesetsa kusintha anthu a dziko lonse lapansi, tiyenera kuyenda ndi Madani Qafilah ﴿عَلَيْهِ الْكَفَلَةُ﴾.



Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagaran  
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 7213

Web: [www.maktabatulmadinah.com](http://www.maktabatulmadinah.com) | E-mail: [feedback@maktabatulmadinah.com](mailto:feedback@maktabatulmadinah.com)